



UNDUNA WA ZACHILENGEDWE
Nthambi Yoona za Nyengo ndi Kusintha kwa Nyengo

ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'DZINJA LA 2026 – 2027



MULANJE DISTRICT


Mwachidule

Nyengo ya dzinja ya 2026-2027 ikuyembekezeka kukhudzidwa **ndi El Nino wa mphamvu**. El Nino ndi kutentha koposera muyezo kwa madzi m'dera la pakati chakum'mawa kwa Nyanja ya mchere ya Pacific komwe kumakhudza kagwedwe ka mvula dziko lonse

Mulanje akuyembekezereka kulandira mvula ya **mulingo wokhazikika kapena kuchepera apo** mu dzinja la 2026-2027.

October 2026

OCTOBER 2026 RAINFALL FORECAST




Mvula ya chizimalupsya yochepera 50 mm ikuyembekezereka mu bomali.

Mvulayi idzakhala yotsogozana ndi mphepo yamkuntho komanso mphenzi.

November 2026

NOVEMBER 2026 RAINFALL FORECAST




Mulanje akuyembekezereka kulandira mvula yokhazikika kapena yochepera ya mlingo wapakati pa 50 ndi 100 mm.

Tiyembekezere mphepo ya mkuntho komanso mphenzi mu mweziwu.

December 2026

DECEMBER 2026 RAINFALL FORECAST




Mvula yokhazikika kapena kucheperapo ya mlingo wapakati pa 200mm ndi 300mm ikuyembekezereka mu bomali.

Madera oyandikira phiri la Mulanje, pa boma ndi ena opezeka kwa TA Laston, Njema komanso akum'mawa akuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo wapakati pa 300 ndi 400 mm.

Mvula ya mlingo okhazikika ikuyembekezeka sabata yomaliza ya mweziwu

January 2027

JANUARY 2027 RAINFALL FORECAST



Tiyembekezere mvula yochepera mlingo wokhazikika wapakati pa 150 ndi 200 mm.


Koma madera opezeka kwa TA Laston, Njema ndi STA Sunganinzeru akuyembekezereka kulandira mvula yochulukirapo yapakati pa 250 ndi 300 mm

Ng'amba ya sabata imodzi ikuyembekezereka mu mweziwu.

Pali chiopsezo cha ng'amba ya sabata imodzi madera ena

February 2027

FEBRUARY 2027 RAINFALL FORECAST




Madera ambiri m'bomali akuyembekezereka kulandila mvula ya mlingo wa pakati pa 100 mm ndi 150 mm.

Komabe, madera ochepa ozungulira ku dera la TA Laston Njema akuyembekezeka kudzalandila mvula ya mlingo wa pakati pa 150mm ndi 200mm.

Tiyembekezere ng'amba yosaposera sabata imodzi mu mweziwu.

March 2027

MARCH 2027 RAINFALL FORECAST




Mwezi wa March, madera ambiri adzalandira mvula yambiri ya mlingo okhazikika kapena kuposera apo, ya mlingo wa pakati pa 200mm ndi 300mm.

Komabe, mvula ya mlingo wa pakati pa 300mm ndi 450mm, ikuyembekezereka kudzagwa madera ozungulira STA Sunganinzeru, TA Laston Njema ndi Mulanje Mountain Reserve.

April 2027

APRIL 2027 RAINFALL FORECAST



M'mwezi wa April bomali likuyembekezereka kulandira mvula yochepera mlingo wokhazikika wapakati pa 50mm ndi 100 mm.

Komabe, madera a kwa TA Laston Njema ndi STA Sunganinzeru akuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo wa pakati pa 100mm ndi 150mm.

Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kudzafika kumapeto sabata loyamba la mweziwu.

DZINJA MWACHIDULE

Kuyamba kwa dzinja

Sabata yomaliza ya mwezi wa December

Ng'amba

Ng'amba ya sabata imodzi mu mwezi wa January ndi February.


Kutalika kwa dzinja

Masiku a pakati pa 100 ndi 110

Kutha kwa dzinja

Sabata yoyamba ya mwezi wa April

MONTH	NORMAL RANGE		FORECAST
OCT	19.5	69.2	40.5
NOV	98.4	138.7	112.9
DEC	188.7	329.7	283.6
JAN	223.7	401.1	237.7
FEB	214.1	271.1	164.2
MAR	166.8	291.2	355.7
APR	65.0	160.8	133.5



Zithunzi izi zapereka ndondomeko ya kagwedwe ka mvula ya pamwezi ya Mimosa

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:



Tsatilani ulosi ndi malangizo ochokera ku nthambi yoona zanyengo



For further information contact:

The Director of Climate Change and Meteorological Services,
P.O. Box 1808, Blantyre.



+265 991 69 00 61

metdept@metmalawi.gov.mw

www.metmalawi.gov.mw